COMPETITION AND FAIR TRADING COMMISSION



MAFUNSO OMWE AMAFUNSIDWA KWAMBIRI OKHUDZA KUPHATIKIZANA KAPENA KUGULANA KWA MAKAMPANI

Chifukwa Chiyani Pali Lamulo Loyang'ana kuphatikizana kwa Makampani?

Kuphatikizana kwa makampani ndikofunika kwambiri pa kayendetsedwe ka chuma cha dziko. Izi zimathandiza makampani kuti aziyenda bwino, azipanga katundu wochuluka pa mtengo wotsika komanso adzichepetsa ziwopsezo ku makampani munjira zosiyanasiyana. Kuphatikizana kumathandizanso kudzutsa makampani omwe anagwa.

Ngakhale izi zili chonchi, kuphatikizana kwa makampani kumasokonezanso mpikisano pa malonda. Kuphatikizanaku kumasokonezanso m'mene makampani amapikisanirana pa msika. Izi zimapweteka wogula malonda. Pofuna kupewa izi, lamulo lowona Mpikisano ndi chilungamo pa malonda limawunikira mmene kuphatikizanako kukuyenera kuyendera kudzera mukupempha chilolezo ku bungwe la CFTC.

Bungwe la CFTC limawunika za m'mene mgwirizano wa makampani ungasinthire mpikisano pa malonda komanso nkhani za chuma. Bungweli limawunikanso bwino komanso limavomera kapena kukana pempho loti makampani aphatikizane.

Kodi kuphatikizana kwa Makampani ndi chani?

Lamulo limati kuphatikizana ndi:

(a) Pamene munthu kapena kampani yagula masheya wochuluka kuposa eni masheya ena onse, kapena kugula zipangizo zomwe kampani ina imagwiritsa ntchito popanga katundu kapenanso pogulitsa katundu wofanana ndi katundu yemwe wogula masheyayo amapanga (Horizontal Merger).

(b) Pomwe munthu kapena kampani yagula masheya wochuluka kuposa eni masheya ena wonse mu kampani yomwe imagulitsa katundu ku kampani kapena munthu amene wagula masheyayo, kapena kugula masheya wochuluka kuchokera ku kampani kapena munthu amene amagulitsa katundu wopangidwa ndi munthu amene wagula masheya wochulukayo (Vertical Merger).

Kodi ndi kuphatikizana kuti komwe kumayenera kuvomerezedwa ndi bungwe la CFTC?

Lamulo silinena za mulingo womwe ungagwiritsidwe ntchito pamene bungwe la CFTC likupereka chilolezo. Izi zikutanthauza kuti bungwe la CFTC liyenera kudziwitsidwa za kuphatikizana kuli konse komwe kukugwirizana ndi tanthauzo la lamuloli polemba kalata.

Kodi bungwe la CFTC liyenera kudziwitsidwa nthawi yanji za kuphatikizana?

Lamulo silinena za nthawi yomwe ma kampani omwe akufuna kuphatikizana ayenera kudziwitsa bungwe la CFTC. Ngakhale zili chonchi, bungwe la CFTC liyenera kudziwitsidwa za kuphatikizana pomwe mbali zokhudzidwa zagwirizana zophatikizana koma zisanamalize ndondomeko yophatikizana. Onesetsani kuti mwadziwitsa bungwe la CFTC mwachangu pomwe ndondomeko

Just Competition, fair Trading
Just Competition, fair Trading

za kuphatikizana zakwaniritsidwa powopa kuphwanya lamulo.

Kodi akuyenera kupempha chilolezo choti makampani aphatikizane ndi ndani?

Wina aliyense atha kukapempha chilolezo ku bungwe la CFTC kuti aphatikizane. Yemwe angatenge chilolezo atha kukhala:-

- Wambali imodzi yofuna kuphatikizana;
- Mbali zonse zofuna kuphatikizana zitha kupempha limodzi; kapena
- Wowayimira pa milandu kapena wowathandizila yemwe mbali zonse zofuna kuphatikizana zasankha.

Mbali zonse zofuna kuphatikizana zikulimbikitsidwa kuti zitenge uphungu ku bungwe la CFTC zisanapemphe chilolezo.

Bungwe la CFTC lidzapereka uphungu potengera uthenga womwe bungweli lalandira kuchokera kwa omwe akufuna kuphatikizana. Bungweli litha kulangiza ofuna kuphatikizanawa kuti apemphe bungwe la CFTC kuti liwunike ngati kuphatikizanako sikukuphwanya lamulo kapenanso ngati kuphakitizanako ndikwathunthu.

Chilolezo choti kuphatikizanako sikukuphwanya lamulo chimaperekedwa kafukufuku akawonetsa kuti kuphatikizanako sikungasokoneze mpikisano pa malonda.

Ofuna kuphatikizanawa amalangizidwa kuti agwiritse ntchito fomu yopemphera chilolezo ndikupereka ku bungwe la CFTC pamodzi ndi ndalama yomwe imayenera kuperekedwa popempha chilolezocho mogwirizana ndi mamulo owona za mpikisano pa malonda.

Kodi kuphatikizana kumawunikiridwa bwanji?

Bungwe la CFTC limawunika pempho lina lili lonse lomwe lalandira ngati pempholo lingakhudze mpikisano pa malonda komanso chuma cha dziko. Ganizo lovomera kapena kukana pempho lofuna kuphatikizana limatengera kuchuluka kwa ubwino kapena mavuto omwe kuphatikizanako kungabweretse pa msika.

Ndi zilango ziti zomwe zimaperekedwa kwa omwe sanapemphe chilolezo kuti aphatikizane?

Wina aliyense yemwe wabisira bungwe la CFTC za kuphatikizana pa nkhani ya malonda apalamula mulandu. Zomwe zidzachitike mulanduwu ukapalamuridwa ndi izi:

- Kuphatikizanako sikudzakhala kovomerezeka pa maso pa lamulo ndipo maufulu wonse womwe kuphatikizanako kumapereka sadzagwira ntchito.
- Onse olowa mu m'gwirizanowu adzayenera kupereka chindapusa cha **MK500,000 kapena ndalama yogwirizana ndi phindu lomwe apeza polakwira lamuloli ngati phindulo linali lochuluka, komanso akakhala kundende kwa zaka zisanu.**

Mukafuna kudziwa zambiri,

Funsani polembera kalata kwa:

HEAD OFFICE

Executive Director
Competition and Fair Trading Commission
New Golden Peacock Office Complex, City Centre
Off Presidential Way 6th Floor
Private Bag 332
City Centre
Lilongwe

Kapena imbani lamya pa:
Tel: +265 310 001 440
+265 310 001 441
Lamya yolipira : +265 1 759506/7

Muthanso kutipeza ku:

REGIONAL OFFICE
Government Building
3rd Floor, Right Wing
Pafupi ndi Unduna wa Zamalonda ndi zokopa alendo
Blantyre

Tel: +265 880 725 075

competitioncommission@cftc.mw
consumer@cftc.mw

www.cftc.mw

CFTC Malawi

Competition and Fair Trading Commission of Malawi

Just Competition, fair Trading
Just Competition, fair Trading